

Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

Za nthawi yopemphera

1. Citanthauzo ca kupemphera
2. Kupemphera m'dzina la Yesu
3. Kumene tiyenera kupemphera
4. Makhalidwe pa nthawi yopemphera
5. Zimene tiloledwa kupempha pa nthawi yopemphera
6. Njira zimene Mulungu ayankha mapemphero
7. Pemphero lofunikira koposa

Pempherani kosaleka 1 Atesalonika 5.17

Mbali zina za m'buku iri zinasandulidwa kucokera ku buku ilo: Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.

1. Citanthauzo ca kupemphera

Atate wathu wa Kumwamba, Dzina lanu liyeretsedwe – Mateyu 6.9b

Kuwerenga

Afilipi 4.6 ndi 7

Malongosoledwe

Kodi mukumbukira zimene tinaphunzira za Mulungu? Kuti ndiye wamkulu kwambiri ndi woyera kwambiri? Ndiponso kuti lye ndi wamphamu zonse, woona zonse ndi wodziwa zonse?

Ife ndife anthu ang'ono ndi ocimwa komabe tiloledwa kulankhula ndi Mulungu wamkulu ndi woyera kwambiri. Pamene tipemphera, tilankhula naye. Ndipo lye akumva. Ndi cinthu codabwitsa!

Mulungu Atate ndi Atate wake wa Yesu komanso Atate wathu. Yesu ndi Mwana wapadera wa Mulungu. Pamene Yesu anali pa dziko lapansi, lye anapempha Atate wake kawiri-kawiri. Nthawi zina duwa lisanaturuke, Yesu anauka m'mawa-mawa kukapemphera. Anakonda kukhala Yekha kuti alankhule ndi Atate wake. Nthawi zina lye sanagone. Tsiku lina anakwera phiri m'usiku nalankhula ndi Mulungu usiku wonse.

Mulungu wa Kumwamba ndiyenso Atate wathu ngati tikhulupirira Yesu. Ndipo afuna kuti tilankhula naye. Afuna kuti timuuza zonse za ife: zimene tikonda ndi zimene tacita. Cimodzi-modzi monga makolo athu afuna kuti tiwauza zonse. Tiyenera kupemphera kwa Mulungu Atate wa Kumwamba nthawi zambiri.

lye atikumvera. Ndipo ife tiyenera kumumvera, monga tiyenera kumvera makolo athu pamene tilankhula nao. Atate wathu wa Kumwamba atiyankha. Sitikhoza kumva mau ake, koma atiyankha m'Baibulo ndilo Mau ake. Ndipo nthawi zambiri atiyankha pamene Mzimu Woyeru alankhula nafe m'mitima yathu.

Tsiku lina ophunzira a Yesu atamuona popemphera, iwo ananena, 'Ambuye, tiphunzitseni kupemphera'. Iwo anadziwa kuti Mulungu ndi wamkulu ndipo sanadziwe kupemphera motani. Yesu anapatsa citsanzo ca pemphero:

*Atate wathu wa Kumwamba,
Dzina lanu liyeretsedwe.*

Ufumu wanu udze.

Kufuna kwanu kucitidwe, monga Kumwamba comweco pansi pano.

Mutipatse ife lero cakudya cathu calero.

Ndipo mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso takhululukira amangawa athu.

Ndipo musatitengere kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woipayo.

cifukwa wanu uli ufumu ndi mphamu ndi ulemerero wa nthawi zonse. Amen.

Tiyenera kupemphera m'njira imeneyi: poyamba kulemekeza Mulungu, kenaka kumpempha zosowa zathu, kenaka kumlemekezanzo.

Kukambirana

1. Kodi mumapemphera?
2. Ndi cifukwa ciani kulankhula ndi Mulungu ndiko cinthu codabwitsa?
3. Ndi cifukwa ciani ophunzira a Yesu anamfunsa kuwaphunzitsa kupemphera?
4. Kambiranani za citsanzo ca pemphero cimene Yesu anatipatsa. Kodi afuna kuti tizipempha ciani?

Citsanzo ca pemphero

Mulungu wa Kumwambawamba, Tikuyamikani cifukwa inu ndinu wamkulu ndi woyera. Zikomo kwambiri kuti mutilola kulankhula nanu. Sitimvetsa kuti mukhoza kutimva, koma tidziwa kuti ndinu wodabwitsa. Conde, tipatseni zimene tisowa m'miyoyo yathu. Tithandizeni kukumverani ndi kukulemekezani nthawi zonse. M'dzina la Yesu tikuphempani izi. Amen.

2. Kupemphera m'dzina la Yesu

Yesu ananena:

Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa – Yohane 16.23b

Kuwerenga

Afilipi 2.9-11

Malongoledwe

Kodi mudziwa nthano ya mkazi wamkulu wa mfumu Ahaswero?

Estere anali mkazi wamkulu wokongola. Analu m'modzi wa anthu a Mulungu (Aisrayeli). Koma mfumu Ahaswero sanali m'modzi wa anthu a Mulungu.

Tsiku lina mtumiki woipa wa Ahaswero anafuna kupha anthu onse a Mulungu. Dzina lake ndi Hamani. Iye anawada Aisrayeli. Ndipo mfumu Ahaswero anaiza Hamani woipa kuti aloledwa kucita kalikonse komwe afuna. Mfumu anakonda Hamani.

Moredekai ndi amene analera Estere, cifukwa Estere anali mwana wamkazi wa atate wake wamng'ono. Moredekai anamva za ciwembu ca Hamani. Iye ndi anthu onse a Mulungu anamva cisoni kwambiri. Koma mkazi wamkulu Estere sanadziwe zimene Hamani anafuna.

Estere atamva za cisoni ca Moredekai, anatuma mtumiki kumfunsa zimene zidacitika. Moredekai anamuza za ciwembu ca Hamani. Ndipo ananena, 'Ndinu mkazi wamkulu. *Inu* tuyenera kupita kwa mfumu kukamfunsa kuletsa Hamani kucita coipa ico'.

Moredekai anaganiza kuti mwina Mulungu anapangitsa Estere kukhala mkazi wamkulu kuti acite tero.

Estere anamva mantha poganzira kupita kwa mfumu. Anati kwa Moredekai, 'Mfumu salola munthu wina aliyense kubwera, koma iye amene aitanidwa. Ndikapita kwa iye, ndidzafadi, pokhapokha iye adzandilozera ndodo yacifumu yagolide.'

Koma kunalibe njira ina yopulumutsa anthu a Mulungu. Ndiye Estere anapita kwa mfumu. Anamva mantha kwambiri. Koma mfumu anakondwera pomuona. Anasekerera nakumulozera ndodo yake yacifumu. Ananena, 'Kodi mufuna ciani, Estere mkazi wamkulu?'

Kenaka Estere anafunsa mfumu kumuthandiza ndipo motero anapulumutsa anthu ake.

Ngati Estere anamva mantha popita kwa mfumu amene anali munthu wamba, ife tiyenera kumva mantha popita kwa Mfumu wa mafumu amene ali Ambuye Mulungu wa zonse za pa dziko lapansi ndi Kumwamba. Ndipo tikumva mantha pamene tikumbukira ukulu wa Mulungu ndi ciyero cake ndiponso kuti ndife ang'ono ndi ocimwa.

Koma sitiyenera kumva mantha ngati tipita kwa lye m'njira moyenerera. Mulungu anatipangira njira. Njira yake ndi yodabwitsa kuposa ndodo yacifumu imene mfumu Ahaswero inalozera kwa Estere mkazi wamkulu. Ife tiloledwa kupita kwa Mulungu *m'dzina la Yesu*. Kodi mukumbukira kuti Yesu anati kwa ophunzira ake kuti, 'Ine ndine Njira?' lye yekha ndiye Njira yopita kwa Mulungu. Sitikhoza kupita kwa Mulungu koma m'dzina lake cabe. Komanso, Ahaswero anali mfumu wankhanza ndi woipa. Mulungu ndi wodekha mtima ndi wacikondi.

Tsiku lina Yesu anati kwa ophunzira ake, '*Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa*' (Yohane 16.23).

Lonjezo iri ndi lodabwitsa.

Kodi kupemphera m'dzina la Yesu kutanthauza ciani? Kutanthauza kuti tikhala otsimikiza kuti Yesu anatifera.

Kutanthauza kuti macimo athu ndi okhululukidwa cifukwa ca Yesu.

Kutanthauzanso kuti mitima yathu ndi yodzala ndi cikondi ca lye ndiponso kuti tizipempha zinthu zomkondweretsa Yesu cabe.

Pamene tipemphera motere, Mulungu Atate akondwera pamene tibwera kwa lye.

Kukambirana

1. Kodi Njira yeni-yeni yopita kwa Mulungu ndi yani?
2. Ndi cifukwa ciani tiyenera kupemphera m'dzina la Yesu?
3. Kodi mumapemphera m'dzina la Yesu?

Citsanzo ca pemphero

Ambuye Mulungu wacisomo, Sitikhoza kubwera kwa Inu mwa mphamvu yathu, cifukwa ndife anthu ocimwa. Tikuyamikani kuti munatuma Yesu kukhala Njira yopulumutsa anthu ocimwa. Zikomo kwambiri kuti mutilola kupemphera m'dzina lake. Yesu yekha ndi ciyembekezo cathu. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi. Amen.

3. Kumene tiyenera kupemphera

Cifukwa cake ndifuna kuti amunawo apemphera pa malo ponse, ndi kukweza manja oyera, opanda mkwiyo ndi makani – 1 Timoteo 2.22

Kuwerenga

1 Mafumu 8.22-28

Malongosoledwe

Solomo anali mfumu wanzeru kwambiri. Ndipo analinso wolemera. Anamanga Nyumba (kapena Kacisi) yooneka bwino ya Mulungu.

Mulungu anacha Nyumbayo ‘Nyumba yopemphereramo’.

Pamene Nyumba yooneka bwino inamangidwa, mfumu Solomo anaitana Aisrayeli onse kubwera ku Yerusalemu.

Tsiku limenelo linali tsiku lokondweretsa. Anthu anakhamukira m’Yerusalemu. Onse anakwera phiri kukaona Nyumba yokongola. Anapereka nsembe monga mphatso za Mulungu. Anaimba matamando a Mulungu. Ndipo anapemphera.

Anthu onse anapemphera pamodzi. Mfumu Solomo anaima pa malo omwe anthu onse anamuonako. Anakweza manja ake ku Mwamba. Anati, ‘Ambuye Mulungu wa Israyeli, kulibe Mulungu monga inu Kumwamba kapena pa dziko lapansi’. Analemekeza Mulungu ndi mtima wake wonse.

Kenaka mfumu anagwada pa maso pa Mulungu. Anatsogolera anthu popemphera ndipo anapemphera nthawi yitali. Kunali zambiri zomwe iye anafuna kunena kwa Mulungu ndi kumufunsa. Anapempha Mulungu kuti adalitse anthu ake ndiponso kuti adalitse ‘Nyumba yopemphereramo’ yooneka bwino.

Masiku ano tiribe Nyumba ya Mulungu. Tiri ndi macalichi. Nthawi zina tingawache ‘nyumba zopemphereramo’. Tidziwa kuti Mulungu ali momwemo ndipo kuti atimva pamene timupempherera momwemo.

Koma tingamupemphera pa malo enanso. Tingapemphera pamene tiri kunyumba. Tingapemphera ku sukulu. Tingapemphera pamene tiri kusewera kapena kuyenda pa mseu. Mulungu ali ponseponse. Tingapemphera paliponse.

Calichi ndi malo apadera a mapemphero, cifukwa m’calichi anthu a Mulungu amapemphera pamodzi. Mulungu akondwera pamene anthu ake asonkhana kukapemphera.

Nthawi zina tingapemphera ndi makolo athu. Nthawi zina banja lonse lipemphera pamodzi. Kukonda Mulungu ndi kumpempha pamodzi monga banja ndi kokondweretsa ndi kodabwitsa.

Koma mungapempherenso pamene muli nokha. Paliponse pomwe mulipo, mukhoza kupemphera. Mulungu akumva pemphero lanu, paliponse pomwe mulipo. Muyenera kupemphera nokha makamaka usiku musanagone mukagwada pansi pa bedi lanu pamene Mulungu yekha akuonani. Kumbukirani kuti usiku Yesu anapemphera mogwada pansi m’mdima.

Kukambirana

1. Kodi mfumu Solomo anacita ciani pamene Nyumba inamangidwa?
2. Ndi cifukwa ciani mfumu Solomo anafuna anthu onse kubwera ku Nyumba ya Mulungu?
3. Kodi mumapemphera kuti?
4. Kodi mumapemphera pamodzi ndi banja lanu?
5. Ndi kuti kumene mwapemphera nokha lero?

Citsanzo ca pemphero

Mulungu wamkulu, Ndi cinthu codabwitsa kuti mutimva pamene tipemphera paliponse pomwe tiripo. Tithandizeni kukumbukira kuti tiyenera kupemphera masiku onse. Tikupemphani izi mwa cisomo, m’dzina la Yesu. Amen.

4. Makhalidwe pa nthawi yopemphera

*Pemphani ndipo mudzalandira, kuti cimwemwe canu
cikwaniridwe – Yohane 16.24*

Kuwerenga

Salimo 95.1-6

Malongosoledwe

Kodi mumaika manja anu pamodzi ndi kutseka maso anu pamene mupemphera?

Njira imeneyo ndi njira yabwino yopemphera. Pamene tiika manja athu pamodzi tiwaletsa kucita zinthu zosayenera pa nthawi yolankhula ndi Mulungu.

Pamene titseka maso athu, tiwaletsa kuona zimene siziri bwino pa nthawi yopemphera. Timaike manja athu pamodzi ndi kutseka maso athu kuti tiganizira za Mulungu ndi zimene tikambira naye cabe.

Koma nthawi zina tingafune kupemphera kopanda kutseka maso ndi kuika manja athu pamodzi.

Nehemiya anali m'modzi wa anthu a Mulungu. Anakhala kutali ku Perisiya. Analis mtumiki wa mfumu wa Persiya. Ankapereka vinyo kwa mfumu.

Tsiku lina mbale wa Nehemiya anabwera kumuona. Nehemiya anamfunsa za anthu a Mulungu ndi mzinda wa Mulungu ndiyo Yerusalem.

Mbale wake ananena, ‘Anthu ndi osauka kwambiri ndi obvutika. Zipupa za Yerusalem zinagwa pansi. Zipata zinatenthedwa.’

Nehemiya anamva cisoni kwambiri pokumva ico.

Pamene Nehemiya anapita kwa mfumu kumpereka vinyo, mfumu ananena, ‘Ndi cifukwa ciani muoneka wosasangalala kwambiri, Nehemiya? Kodi mtima wanu wabvutika?’

Nehemiya anayankha, ‘Sindingacite kena kalikonse koma kuoneka wacisoni, mfumu. Mzinda wa anthu anga ndi woonongeka ndipo zipata zinatenthedwa’.

Mfumu ananena, ‘Kodi mungakonde kucita ciani?’

Pa nthawi imeneyo Nehemiya anapemphera. Pamenepo pamene anaima pa maso pa mfumu, iye anapempha Mulungu. Sanakhoze kugwada pansi kapena kuika manja ake pamodzi ndi kutseka maso ake. Anangoima pomwepo. Anapempha Mulungu kuti mfumu akhale wabwino ndi wodekha mtima.

Ndipo pamene anali kupemphera, iye anati kwa mfumu, ‘Cikakomera mfumu, ndifuna kupita ku dziko langa. Ndingakonde kuthandiza anthu anga kumanga mzinda.’

Ndipo mfumu analola Nehemiya kupita. Mulungu anayankha pemphero la Nehemiya. Mfumu anatumwa asirikali kupita ndi Nehemiya.

Mulungu anapangitsa mfumu kukhala wabwino ndi wodekha mtima, monga Nehemiya anapemphera pamene anali kulankhula ndi mfumu.

Nehemiya sanapemphera komveka. Anapemphera m'mtima mwake. Ndi Mulungu Yekha amene anakhoza kumva pempherolo. Mfumu sanalimva konse.

Ifenso tingapemphera m'mtima yathu kopanda kuika manja athu pamodzi ndi kutseka maso. Tingapemphera pamene tiri kusewera. Tingapemphera pamene cinthu citicititsa mantha cicitika mwadzidzidizi. M'njira imeneyi tiyenera kupemphera nthawi zambiri.

Nthawi zina tigwada pansi pamene tipemphera. Nthawi zina tikhala pansi. Koma tingapemphera ngakhale tiri kuyenda kapena kugwira nchito. Kupemphera nthawi zambiri kudzatisandukitsa Akristu osangalala.

Kukambirana

1. Kodi kupemphera m'mtima kutanthauza ciani?
2. Kodi Mulungu amamva mapemphero osamveka ndi anthu?
3. Ndi cifukwa ciani nthawi zina tiyenera kugwada pansi pa nthawi yopemphera?
4. Kodi pemphero likwaniritsa kutisangalatsa motani?

Citsanzo ca pemphero

Mulungu wodabwitsa, Zikomo kwambiri kuti mukumva mapemphero onse. Mudziwa zimene ziri m'mtima yathu. Tikuphunzitseni kukhala ndi miyoyo yopemphera nthawi zonse. M'dzina la Yesu tikuphemphani izi. Amen.

5. Zimene tiloledwa kupempha pa nthawi yopemphera

Mupempherere wina kwa mnzace – Yakobo 5.16b

Kuwerenga

2 Mafumu 19.14-19

Malongosoledwe

Kuli zinthu zambiri zomwe tifuna kukhala nazo! Kodi tiloledwa kupempha Mulungu kalikonse komwe tifuna?

Zoona, anthu a Mulungu samupempha konse zinthu zoipa. Sitipempha konse Mulungu zinthu zimene tidziwa kuti ndizo zoipa.

Tiloledwa kumupempha ciriconse cimene tisowa ndi cimene tifuna pokhapo ngati tiganiza kuti ciri bwino kwa ife.

Baibulo litiuza za mfumu Hezekiya wa kale. Mfumu Hezekiya anali munthu wabwino. Anakonda Mulungu ndipo anayesa kucita cifuniro ca Mulungu.

Tsiku lina mfumu woipa anabwera kuthirana nkhondo ndi Hezekiya. Analu ndi asirikali abwino. Anati kuti adzatenga zonse zimene Hezekiya anali nazo. Anafuna kutenga ngakhale mzinda wa Mulungu (Yerusalem) nanena kuti mzindawo uli wake.

Hezekiya anakhulupirira mwa Mulungu. Koma mfumu woipa anapereka kalata kwa Hezekiya. M'kalata iye ananena, 'Musakhulupirire Mulungu wanu. Mulungu wanu sakhoza kukupulumutsani. Asirikali ambiri anga adathirane nkhondo ndi anthu ena ambiri. Iwo anapempha milungu yao, koma milungu yao sanakwaniritse kuwapulumutsa. Ndipo Mulungu wanu sakwaniritsa kukupulumutsani.'

Hezekiya anaganiza za mfumu woipa ndi asirikali ake ambiri ndi amphamu. Anadziwa kuti iye yemwe anali ndi asirikali ocepa kuti angapambane asirikali a mfumu. Ndiye Hezekiya anapita kwa Nyumba ya Mulungu kukapemphera ndi kupempha Mulungu kuti amthandize. Anagwada pansi m'Nyumba ya Mulungu nafunyulula kalata pa maso pa Mulungu.

Hezekiya anapemphera, 'Onani, Mulungu. Onani zoipa zimene mfumu woipa anena za Inu. Zonse zimene anena za milungu ina ndi zonna. Milungu ina sinapulumutse anthu awo. Sinakhoze, cifukwa iwo ndiwo mafano. Koma inu ndinu Mulungu wamoyo. Kulibe Mulungu koma inu nokha. O, titandizeni ndi kutipulumutsa!'

Mulungu anakondwera ndi pemphero la Hezekiya. Anapulumutsa Hezekiya, mzinda ndi anthu ake onse. Anatuma mngelo kucititsa mantha mfumu woipa ndi asirikali ake. Usiku uja asirikali onse anathawa.

Mulungu afuna kuti timuuza zimene zitibvutitsa. Afuna kuti timpempha thandizo. Kumbukirani kuti lye ndi Atate wathu. Pamene tithamanga kwa makolo athu, atithandiza. Atate wa Kumwamba atithandizano pamene tipita kwa lye m'pemphero.

Afuna kuti timpempha ciriconse cimene tisowa, ngakhale cimene tingakonde kukhala naco koma siticifunikadi.

Kukambirana

1. Kodi mwapelema ciani kwa Mulungu lero?
2. Kodi mumadzipempherera kapena mupempherera anthu ena?
3. Patsani zitsanso zisanu za anthu omwe tingapemphererek.
4. Kodi Mulungu amayankha mapemphero onse?

Citsanzo ca pemphero

Mulungu wacifundo, Zikomo kwambiri kuti mutilola kukupemphani zimene tisowa m'miyoyo yathu. Mudziwa zonse. Mudziwa mabvuto athu. Mudziwa matenda athu. Tikupemphani kuti mutidalitse ndi zonse zimene tifunika kuti tiphunzire kukulemekezani m'zonse. Tikuyamikani pa zonse zimene mumatipatsa. M'dzina la Yesu tikupemphani izi. Amen.

6. Njira zimene Mulungu ayankha mapemphero

*Koma Mulungu wanga adzakwaniritsa cosowa canu ciri conse monga mwa cuma cace m'ulemerero
mwa Kristu Yesu – Afilipi 4.19*

Kuwerenga

Salimo 66.16-20

Malongosoledwe

Timapempha zinthu zambiri ku makolo athu. Kodi makolo amatipatsa zimene tiwapempha nthawi zonse? Iai! Nthawi zina aganiza kuti kwabwino koposa ndi kuti sitipatsidwa zimene tawapempha. Nthawi zina iwo sakwanitsa kutipatsa. Nthawi zina sakhoza kutipatsa.

Cimodzi-modzi Mulungu satipatsa pempho lathu nthawi zina. Mulungu akhoza kutipatsa, koma nthawi zina sapatsa.

Kuli zifukwa zambiri zimene Mulungu satipatsira zimene timpempha.

Ngati tipempha Mulungu titakhala osamvera ndi kukhala osakhululukidwa ku chimolo, Mulungu sayankha pemphero lathu. Poyamba tiyenera kumpemphera cikhululukiro ku macimo athu.

Nthawi zina tingopempha zinthu zotikondweretsa cabe. Mulungu sakonda mapemphero otere. Kodi mukumbukira zimene ananena za kukhala odzikonda? Ngati tingodziganizira, ndife odzikonda ndipo Mulungu sayankha mapemphero otere.

Nthawi zina Mulungu satipatsa zimene tampeempha, ngakhale tiganizira kuti tizifunikadi. Paulo, mtumiki wamkulu wa Mulungu, anali ndi ‘minga’. Minga iyi sinali minga yeni-yeni. Inali cinthu cobvutitsa kwambiri Paulo. Mwina cinali uwawa wa pa maso ake. Sitidziwa. Paulo anapempha Mulungu kucotsa ‘mingayo’. Anapemphera katatu. Paulo anaganiza kuti angatumikire kwabwino koposa ngati Mulungu acotsa mingayo ndi kumciritsa.

Koma Mulungu sanacotse minga. Mulungu anati kuti cabwino coposa ndi kuti Paulo akhala nayo. Ndiye Mulungu sanapatse Paulo cimene iye anampempha.

Paulo sanamve cisoni pa ico. Anadziwa kuti cifuniro ca Mulungu ciri cabwino coposa. Paulo anadziwa kuti Mulungu amacita zimene ziri zabwino zoposa kwa ana ake.

Makolo athu amayesa kuticitira zabwino. Nthawi zambiri satipatsa zimene tiwapempha, cifukwa zinthu zimenezo siziri zabwino. Mulungu adziwa bwino kwambiri kuposa makolo athu zimene ziri zabwino kwa ife ndi zimene si ziri zabwino. Ngakhale Yesu anapemphera, ‘Kufuna kwanu kuditidwe’.

Mulungu amatimva pamene tipemphera. Koma nthawi zina satipatsa zimene timpempha. Nthawi zina anena, ‘Iai, ico si cabwino kwa inu’. Nthawi zina anena, ‘Yembekezani. Musakhale naco tsono’. Adzatipatsa ngati cimene tampeempha ciri cabwino kwa ife. Tiziphunzira kukhulupirira Mulungu.

Kukambirana

1. Kodi mumapemphera modzikonda?
2. Kodi mumapempha Mulungu cikhululukiro ca macimo anu?
3. Kodi kukhulupirira Mulungu kutanthauza ciani?
4. M’Aroma 8.26 tiwerenga, ‘Ndipo momwemonso Mzimu (Woyer) athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwina atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka.’ Kodi ndime iyi itanthauza ciani?

Citsanzo ca pemphero

Mulungu wa Kumwamba, Nthawi zambiri tipemphera moipa. Tiphunzitseni kupemphera kwabwino. Tiphunzitseni kupemphera kulingana ndi cifuniro canu. Tikupemphani kuti mutipatse Mzimu Woyer ake, ‘Ndipo momwemonso Mzimu (Woyer) athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwina atipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka.’ Amen.

7. Pemphero lofunikira koposa

Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace – Mateyu 6.33a

Kuwerenga

Mateyu 6.25-33

Malongosoledwe

Mulungu afuna kuti timpempha zimene tisowa. Tifunika cakudya, zobvala ndi nyumba. Izi ndi zofunikira kwambiri. Koma kuli cinthu cofunikira coposa.

Tsiku lina Yesu ndi ophunzira ake anakwera phiri. Yesu anakhala pansi pa msipu naitana ophunzira ake kukhala pafupi naye. Mbalame zinali kuimba. Mbalame zina zinali kudy tizirombo ta m'mpweya, zina zinali kuyenda pa dziko kukapeza nyongolotsi ndi tizirombo tina. Maluwa ooneka bwino anakhala pa msipu. Tsiku limenelo linali labwino kuti anthu akhale pabwalo ndi kumvera Yesu.

Poyamba Yesu anauba ophunzira ake kuti kupezedwa m'Ufumu wa Mulungu ndi kodabwitsa. Aliyense wokhala momwemo ndi wodalitsika. ‘Odala osauka a mumzimu’, anati Yesu, ‘cifukwa uli wao Ufumu wa Kumwamba’. Ndipo ‘Odali ali akucita mtendere’. Ndipo ‘Odala ali oyera mtima’.

Kenaka Yesu anafotokoza njira m'mene anthu a Mulungu ayenera kukhala miyoyo yao kwa Mulungu, momwe anthuwo ayenera kukhala ndi zimene ayenera kucita.

Yesu ananena, ‘Musadere nkawa za kukhala ndi cakudya cokwanira kapena zobvala zokwanira. Yang'anirani mbalame. Atate wanu wa Kumwamba adyetsa mbalame ndipo inu muli kusiyana nazo kuziposa. Adzakudyetsani ndithu.’

‘Ndipo yang'anirani maluwa. Onani kukongola kwao. Mulungu anawakhulitsa masamba ao kuti aoneke abwino oposa zobvala zonse za mfumu Solomo. Adzakubvalitsani ndithu!’ Mudziwa kuti atikonda, iai?

Kenaka Yesu ananena, ‘Musaganizire zobvala ndi ndalamu nthawi zonse. Izi sizikhala ndipo njenjete kapena dzimbiri iziononga. Anthu osadziwa Mulungu amaganizira zinthu zimenezo. Koma cofunikira coposa ndi kuti, ‘Muthange mwafuna Ufumu wa Mulungu’.

Pamene Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kupemphera, lye anati kuti ayenera kunena, ‘Ufumu wanu udze’ (Mateyu 6.10). Kupempherera Ufumu wa Mulungu ndi kofunikira kuposa kupempha cakuda, zobvala kapena cina cimene tisowa. Kupempha kuti Ufumu wa Mulungu udze ndi pemphero lalikulu loposa. Ndipo Yesu anati kuti tikaika Ufumu wa Mulungu kutsogolo, tidzapatsidwa zina zonse zomwe tifunika. Ici ndi lonjezo lake!

Kodi tipempha ciani pamene tiika Ufumu wa Mulungu kutsogolo? Tipempha Mulungu kutipangitsa ngati kuunika kakang’ono kwabwino kowalira kwa lye. Tipempha kuti Mulungu adalitsa atumiki ake kuti anthu ena ambiri adzayamba kukonda Yesu. Tipempherera atsikana ndi anyamata osadziwa Mulungu ndi kucita zinthu zoipa. Kodi mungaganizire zinthu zina zimene tingapemphe Mulungu?

Tisaiwale pemphero lofunikira loposa: Ufumu wanu udze.

Kukambirana

1. Ndi cifukwa ciani kupempha kuti Ufumu wa Mulungu udze ndi kofunikira kwambiri?
2. Ngati ndife m'Ufumu wa Mulungu, ndi yani amene ali Mfumu wathu?
3. Kodi tingaonetse bwanji kuti Mulungu ndi Mfumu m'zonse zimene ticita?

Citsanzo ca pemphero

Mulungu wa Kumwamba, Inu ndinu Mfumu wa mafumu amene alamulira zonse, makamaka Ufumu wanu. Tikupemphani kuti Ufumu wanu udze. Mutembenuze anthu ambiri kuti akhale m'Ufumu wanu. Tikupemphani kuti anthu ena ambiri asanduke ana anu kuti akhale m'Ufumu wanu, kuti muwalalumira. Mutilamulirenso kuti ticita zokondweretsa zanu. M'dzina la Yesu Mpulumutsi tikupemphani izi. Amen.